MBIRI YA KATIKISIMU WA BAIBULO
MBIRI YA CHIPANGANO CHAKALE
KUMASULIRA KWA MALONJEZANO A PANGANO NDI MULUNGU

Akula (Kalasi Yachitatu)
Buku Loyamba La Awiri

Wolemba ndi **Rev. John A. Heys**
Mkonzi ndi **Pastor J. J.Lim**
Wothandizira wapadera ndi **David Higgs**.

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** komanso **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** komanso **Rev. Precious Kanyowa**

February 2011 edition

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Katekisimu wa Mbiri ya M'baibulo- Nkhani za m'Baibulo za Chipangano Chakale
(KUMASULIRA KWA MALONJEZANO A PANGANO NDI MULUNGU)
Ophunzira achikulire- Buku Loyamba La Awiri
Lalembedwa ndi **Rev John A. Heys**
Lakonzedwa ndi **Rev. J.J.Lim**
Mwaonjezeredwanso mfundo zina ndi **Pastor David Higgs**

Latanthauziridwa mu Chichewa ndi **W. Chapasuka** ndi **A. Mkwinda**
Lakonzedwa mu Chichewa ndi **Rev. Rex Chitekwe** ndi **Rev. Precious Kanyowa**

Buku leni leni loyambilira limene anatanthauzira ndi **Rev A. Heys** eni ake ndi a Prostestant Reformed Churches of America
Buku ili lakonzedwanso ndi Rev. J.J. Lim mu 2011 mothandizidwa ndi Pilgrim Covenant Church.

Chichewa version © 2012 Gratia Dei Sola Media
Lasindikizidwa ndi Grata Dei Sola Media
Blk 203B, Henderson Road , #07-07, Singapore 159546
Website: www.gdsmedia.org
Email: gdsmedia.sg@gmail.com

Palibe akuloledwa kusindikiza kapena kuchulukitsa buku ili ngakhale za mkatimu

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Synod ya Evangelical Presbyterian Church (EPC) ku Malawi ndi ku Mozambique inavomereza mu chaka cha 2012 kuti bukuli lizigwiritsidwa ntchito mu mipingo yawo yonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

Mau Otsogolera a Mlembi

Katekisimuyu walembedwa motengera mau opezeka pa Genesesi 3:15 ndiye lonjezo lalikulu, chiyambi cha chipangano cha uthenga wabwino,komanso kuti mbiri yonse ya chipangano chakale ndiye chimasulo cha pangano limenelo.

Pachifukwa ichi, tagawa nthawi yonse kuyambira pa chiyambi cha kulengedwa kwa dziko mpaka kubadwa kwa Yesu Khristu mmagawo asanu ndipo gawo lililonse likuthera mu kupambana kwa mpingo pa nkhani yokwaniritsa lonjezoli. Kupambana kusanu kumeneku ndikupambana kwa chigumula, nyanja yaikulu yofiira, kwa Davide pakati pa adani ake mu dziko lolonjezedwa pamodzi ndi mtendere komanso ulemelero wa ulamuliro wa Solomo, chipambano cha ana a Israeli kuchokera ku ukapolo komanso kupambana kwa kubadwa kwa Yesu Khristu. Kupambana kwa chisanu ndi chimodzi kwaikidwa m'buku lina la akulu lomwe likukamba za kubwera kwa Yesu Khristu pa tsiku lomaliza kuti adzakhadzikitse Sabata la Muyaya.

Tayesesanso kukamba kuti Mulungu wathu wa chipangano ndi wokhulupilika nthawi zonse pa lonjezo lake ngakhale kuti nthawi zambiri mpingo wake umadzionetsa kukhala wosakhulupirika.

Bukuli lakonzedwa kuti lithe kuthandiza mwana kuti azindikire yekha choonadi chomwe adzakhale akuchikumbukira nthawi zonse.

Tikufuna kuthokoza Mbusa G M Ophoff, amene ndi kadaulo wa zamaphunziro a mbiri ya chipangano chakale ku sukulu yotchedwa Theological School of the Protestant Reformed Churches in America, yomwe yathandiza polemba katekisimuyi ndi zonse zopezeka m'bukuli.

Ambuye adalitse zonse zomwe zalembedwa m'bukuli kuti ana athu athe kuphunzira kukonda choonadi choti ," kotero kuti sichifuma kwa munthu amene afuna, kapena kwa iye amene afuna,kapena iye amene athamanga koma kwa Mulungu amene achitira chifundo (Aroma 9:16)

- Rev. J A Heys,1961

Mau Otsogolera a Mkozi

Bukuli (Lomwe latulutsidwa mu February 2011) lakonzedwa mwina ndi mwina kuchokera ku buku lomwe lakhala likugwiritsidwa ntchito ndi a PRC ku America kwa zaka zokwana makumi anayi. Zolakwika zina zayetsedwa kuchotsedwa mounika bwino. Mafunso ndi mayankho ena ndi ena asinthidwa kuti ana athu athe kukumbukira bwino popanda kusintha uthenga wina uliwonse. Mafunso ena amene sanali ogwirizana bwino ndi chiphunzitso cha buku lopatulika komanso amene samatha kufotokoza bwino achotsedwa ndipo mmalo mwake ena ofunikira ayikidwa. Nkhani zina ndi zina zaperekedwa ndi Pastor David Higgs amenenso anaperekapo maganizo awo pa mafunso osiyanasiyana. Ndime zoloweza kapena zapamtima zochokera mu Scottish Psalter zaonjezeredwanso kuti zithandize onse amene sanathe kuloweza mbali zina za Masalimo.

Bukuli ndi lachitatu mmakatekisimu athu okamba za mbiri ya buku lopatulika ndipo makolo adzaona kuti lasintha movutirapo mu makambidwe a nkhani zake molingana ndi kukula kwa ana. Ngakhale izi zili chomwechi, ana ena atha kumvetsa mafunso onse khumi komanso ndime zapamtima. Ngati izi zachitika, ndikufuna kupempha makolo kuti awathandize anawo pobwereza kuloweza Katekisimu wa Wesminister kuti athe kukonzekera katekisimu wina amene akubwera .

Mulungu wamkulu adalitse kuyesetsa ndi kukangalika kwathu pokuza ana molingana ndi mmene pangano lathu lifunira.

- Pastor JJ Lim, 2011

Copyright © Gratia Dei Sola Media

NTHAWI YOYAMBA
Kuchokera Nthawi ya Kulengedwa kwa dziko kufikira
Kupambana kwa Chigumula

PHUNZIRO 1
MULUNGU AMALENGA ZINTHU ZONSE

1. **Nenani vesi yoyamba ya Baibulo.**
   Pachiyambi Mulungu analenga kumwamba ndi dziko lapansi" (Genesesi 1:1).

2. **Kodi kufunika kwake nkotani kuti Buku lathu lopatulika likuyamba ndi vesi imeneyi?**
   Chifukwa ndimeyi imatiphunzitsa kuti Mulungu wathu ndi wosatha ndipo zinthu zonse, zooneka ndi zosaoneka, ndizopangidwa ndi iye. (Masalimo 90:2)

3. **Kodi Mulungu analenga bwanji zinthu zonse?**
   "Pakuti adanena ndipo zinachitika, Analamula ndipo zinakhadzikitsika" (Masalimo 33:9)

4 **Kodi mchifukwa chiyani Mulungu analenga zinthu zonsezi?**
   Chfukwa cha ulemelero wa dzina lake (Chivumbulutso 4:11).

5. **Kodi chinthu chofunika chomwe timawerenga pa za kulengedwa kwa munthu ndi chiyani?**
   Malembo amati, " Mulungu analenga munthu mu chifanizo chake" (Genesesi 1:27)

6. **Kodi munthu analengedwa kuti akhale osiyana ndi zolengedwa zina zonse zapansi?**
   Inde , munthu analengedwa kuti athe kumudziwa Mulungu, kuyankhula naye komanso Kukondana naye (Genesesi 2:7b)

7. **Kodi Mulungu adalenga bwanji munthu?**
   " Yehova Mulungu anaumba munthu ndi dothi lapansi, nauzira mpweya wamoyo m'phuno mwache, munthuyo nakhala ndi moyo" (Genesesi 2:7)

8. **Kodi ubale wa Adam ndi zolengedwa zina zonse unali wotani?**
   " Iye anali ndi ulamliro pa izo motsogozedwa ndi Mulungu" (Genesesi 1:26; Masalimo 8:6-8)

9. **Kodi Adam anali kukhala kuti?**
   M'munda wa Edeni womwe unali chithunzithunzi cha ulemelero wa kumwamba (Mwa chitsanzo, Chivumbulutso 22:1-2)

10. **Kodi ndi mitengo yanji yamtundu wina yomwe inali mmundamo?**
    Mtengo wa moyo komanso mtengo wakudziwitsa chabwino ndi choipa (Genesesi 2:17; 3:24)

Ndime zina zapamtima zoonjezera: Masalimo 145: 1-4.

1. Ndidzakukwezani Mulungu wanga mfumu
   Ndipo ndidzalemekeza dzina lanu kunthawi za nthawi.
2. Masiku onse ndidzakuyamikani;
   Ndikulemekeza dzina lanu ku nthawi za nthawi
3. Yehova ndi wamkulu, ayenera kulemekezedwa kwakukuru:
   Ndi ukulu wake ndi wosasanthulika.
4. Mbadwo wina udzalemekezera ntchito za mbadwo umzache,
   Ndipo udzalalikira zamphamvu zanu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 2
LONJEZO LA UTHENGA WABWINO

1. **Kodi Mulungu anauza Adam chiyani chokhudza mtengo wakudziwitsa chabwino ndi choipa?**
   "Koma mtengo wakudziwitsa chabwino ndi choipa umenewo usadye chifukwa tsiku limene udzadya umenewo udzafa ndithu" (Genesesi 2:17)

2. **Kodi Adam anasunga lamulo la Mulungu limeneli?**
   "Iyayi, chifukwa anadya chipatsochi chomwe mkazi wake Hava anamupatsa" (Genesesi 3:6)

3. **Kodi ndani amene anamunyenga Hava kuti adye chipatsochi?**
   Satana ndiye anamunyenga ndi bodza lakuti ," Iwe sudzafa ayi" (Genesesi 3:4-5)

4. **Kodi Adam ndi Hava anazindikira kuti anali olakwa chifukwa cha tchimo lawo?**
   Inde, poti anazindikira kuti anali amaliseche ndipo anadzisokera masamba amkuyu napanga matewera. (Genesesi 3:7)

5. **Kodi Mulungu anabisa bwanji umaliseche wawo?**
   Yehova Mulungu anawapangira Adamu ndi mkazi wake malaya azikopa nawaveka iwo. (Genesesi 3:21)

6. **Kodi thembelero la Mulungu kwa Adam linali lotani?**
   " Ndipo ndidzaika udani pakati pa iwe ndi mkaziyo, ndi pakati pa mbeu yako ndi mbeu yake, ndipo idzalalira mutu wako ndipo iwe udzalalira chitende chache" (Genesesi 3:15)

7. **Kodi chofunikira ndi chiyani pa nkhani imeneyi?**
   Uku ndi kunenedwa koyamba kwa lonjezo la uthenga wabwino.

8. **Kodi mbeu ya mzimayi ikutanthauza Ana onse a Hava?**
   Ayi, ikukamba za Khristu ndi onse akugwirizana ndi iye. (Agalatiya 3:16; Aefeso 5:30; ndi ena)

9. **Kodi ndi ndani amene Yehova akukamba pamene anena kuti mbeu ya njoka?**
   Mulungu anena anthu amene amadana ndi Iye komanso kudana ndi mpingo wake ndipo nthawi zina amatchedwa mmalemba kuti " a m'dziko." (1 Yohane 3:13)

10. **Kodi Mulungu anakwaniritsa bwanji lonjezo lake?**
    Anatumiza mwana wake kuti adzapulumutse anthu ake ku mphamvu ya satana. (Aroma 16:20)

Ndime zapamtima zoonjezera: Masalimo 145:5-6

5. Ndidzalingalira ulemelero waukulu wa ulemu wanu ndi ntchito zanu zodabwitsa.
6. Ndipo adzanenera mphamvu za ntchito zanu zoopsa; ndi ukulu wanu ndidzaufotokozera.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 3
KUKHADZIKIKA KWA TCHIMO

1. **Kodi chimene chinaonekera poyera mwa ana awiri amene Mulungu anapereka kwa Adam ndi Hava ndi chiyani?**
   Kaini woipayo anali mbeu ya njoka ndipo Abele wolungamayo anali mbeu ya mzimayi. (1 Yohane 3:12, Mateyu 23:35).

2. **Kodi Abele anasonyeza bwanji kuti anali mbeu ya mzimayi?**
   Mwachikhulupiliro anapereka nsembe ya nyama kwa Mulungu ,zimene zinaonetsa chikhulupiliro chake mwa Khristu amene ali nkudza. (Genesesi 4:4; Ahebri 11:4)

3. **Kodi Abele anasonyeza bwanji kuti anali mbeu ya njoka?**
   Ponyozera malangizo a Mulungu mmene ayenera kupembedzera, anapereka nsembe ya chipatso cha mu nthaka komanso anapha Abele amene ankakonda Mulungu. (Genesesi 4:8)

4. **Kodi cholinga cha satana chinali chotani pakupha Abele?**
   Anali kuyesetsa kuletsa kuti Khristu asabadwe. (Genesesi 3:15; onaninso Yohane 3:12)

5. **Kodi Mulungu anapitiliza bwanji mbeu ya mzimayi Abele atafa?**
   Mulungu anamupatsa Adam ndi Hava mwana wina woopa Mulungu amene anamupatsa dzina loti Seti. (Genesesi 4:25)

6. **Kodi kuipa kwa mbeu ya njoka kunadzionetsanso kokha kachiwiri?**
   Inde, popeza kuipa mtima kwa munthu kunachuluka pa dziko lapansi. (Genesesi 6:5)

7. **Kodi Kuipa mtima kwa munthu kunali kwakukulu bwanji?**
   "....chirichonse chomwe mtima wake unali kuganiza chinali choipa nthawi zonse " (Genesesi 6:5)

8. **Tchulani Munthu mmodzi wa m'badwo wa Kaini amene anadzionetsa kukhala mbeu ya njoka?**
   Lameki woipa mtima amene anadzitamandila kwa akazi ake awiri kuti wapha munthu. (Genesesi 4:23)

9. **Tchulani Munthu mmodzi wa m'badwo wa Seti amene anadzionetsa kuti ndi mbeu ya mzimayi**.
   Enoki amene anali kuyenda ndi Ambuye. (Genesesi 5:24)

10. **Kodi mbeu ya mzimayi inamutumikira Mulungu mu mphamvu yawo?**
    Iyayi, "pakuti wakuchita mwa inu kufuna ndi kuchita komwe, chifukwa cha kukoma mtima kwake, ndiye Mulungu." (Afilipi 2:13)

Ndime zapamtima: Masalimo 145: 7 -8

7. Adzabukitsa chikumbukuro cha ubwino wanu waukulu,
   Nadzayimbira chilungamo chanu.
8. Yehova ndiye wachisomo ndi wachifundo;
   Osakwiya msanga ndi wachifundo chachikulu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 4
KUPULUMTSIDWA MU CHOMBO

1. **Kodi mpingo unali waukulu mu nthawi ya chigumula?**
   Ayi, panali mizimu isanu ndi itatu imene inatsala ndi kukhulupilira komanso kumvera Mulungu. (1 Petro 3:20)

2. **Kodi Nowa anaonetsa bwanji kukhulupilira kwake ku anthu a m'dziko osakhulupilirawo?**
   Anaonetsa kukhulupilira kwake pomanga chombo monga mmene Mulungu ananenera. (Ahebri 11:7)

3. **Kodi timamva chiyani za kuipa kwa anthu a panthawiyo?**
   Anali kuchimwa ndikuchita zinthu ngati kuti chigumula sichidzabwera pa iwo. (Mateyu 24:37-39)

4. **Kodi Mulungu anachitira chiyani mpingo wake patsikulo?**
   Anapulumutsa mpingo wake ku chigumula. (1 Petro 3:20)

5. **Kodi ndi lonjezo lanji limene Mulungu anapereka kwa Nowa?**
   Mulungu anati kwa Nowa,".koma ndidzakhadzikitsa ndi iwe pangano langa; ndipo udzalowa m'chingalawamo, kuti zikhale ndi moyo pamodzi ndi iwe,zikhale zamphongo ndi zazikazi. (Genesesi 6:18)

6. **Kodi lonjezoli litanthauzanji?**
   Litanthauza kuti Mulungu adzakhala mnzake komanso adzamupulumutsa iye ndi banja lake mu chombocho. (1 Petro 3:20; Ahebri 11:6-7)

7. **Kodi Mulungu anasunga pangano lake?**
   Inde, Mulungu anaononga onse ochimwa ndi chigumulacho ndikupulumutsa Nowa ndi banja lake. (Genesesi 7: 21-23)

8. **Kodi lonjezoli likukambanso chiyani?**
   Lonjezoli litiuza kuti Mulungu adzapulumutsa mpingo wake kudzera mwa mpulumutsi amene adzamutumize. (1 Petro 3:20-21; Mateyu 1:21;1 Akorinto 12:12-13)

9. **Kodi kupambana kwake kwa chionongeko cha oipachi nkotani?**
   Chifukwa ndi chiombolo chachikulu choyamba chimene Mulungu anapereka ku mpingo wake. (Genesesi 3:15)

10. **Kodi ndi chiyani china chimene chinganenedwe pa zachinongeko cha oipawo mchigumula?**
    Kuli ngati mbali imodzi ya chiweruzo cha pa tsiku lomaliza. (Mateyu 24:37-39)

Ndime zapamtima: Masalimo 145:9

9. Yehova achitira chokoma onse
   Ndi nsoni zokoma zonse zigwera ntchito zake zonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

NTHAWI YACHIWIRI
Mmene linaliri dziko Patatha Chigumula kufikira Kupambana kwa pa nyanja yaikulu yofiira

PHUNZIRO 5
KUBWERERANSO KWA TCHIMO

1. **Kodi tchimo linadzionetsanso bwanji patatha chigumula?**
   Nowa analedzera ndipo mwana wake Hamu anasangalala ndi tchimo la abambo ake. (Genesesi 9:20-22)

2. **Kodi Mulungu akutionetsa chiyani pa machimo a anthu amene anawapulumutsa mu chigumula?**
   Akutionetsa kuti chigumulachi sichinali kutheratu kwa tchimo. (Ahebri 11:7; Aroma 3:21-26)

3. **Kodi ndi chiyani chomwe anthu ochimwawo anachifuna chifukwa cha machimo awo?**
   Anali kufuna mpulumutsi kuti awapulumutse iwo ku machimo awo. (Ahebri 11:13)

4. **Kodi Semu ndi Yafeti anadzionetsa bwanji kuti anali olungama?**
   Iwo sanasangalale ndi tchimo la atate awo monga Ham koma anafunditsa umaliseche wa atate awo ndi chofunda. (Genesesi 9:21-23)

5. **Kodi pali chinthu china chimene chikuonetsa kuti Noah anadana ndi machimo ake?**
   Inde, popeza anadalitsa Semu ndi Yafeti koma anatembelela Kanani, mwana wake wa Hamu. (Genesesi 9:24-27)

6. **Kodi tchimo linakula patatha chigumula?**
   Inde, pakuti oipawo anagalukira Mulungu pomanga nsanja ya Babele. (Genesesi 11:1-4)

7. **Kodi oipawo anamangiranji nsanjayo?**
   Iwo anali kufuna kufanana ndi Mulungu komanso kukhala pamodzi mogwirizana ngati dziko limodzi lamphamvu (Genesesi 11:4)

8. **Kodi Mulungu anathana nazo bwanji izi?**
   Mulungu anawapatsa iwo ziyankhulo zisiyanasiyana ndi kuwamwaza pa dziko lonse lapansi. (Genesesi 11:7-8)

9. **Kodi ndi chifukwa chiyani Mulungu anawamwaza ndi kupanga maiko osiyanasiyana?**
   Kuti mpingo wake ukule bwino m'dziko loipali. (Genesesi 12:1-3)

10. **Kodi anthu osunga pangano la mulungu tiwapeza kuti kuyambira nthawi imeneyi?**
    Mpingo unali kupezeka mu mbumba ya Semu ndipo kenakanso ya Yafeti. (Genesesi 9: 26-27)

Ndime zapamtima: Masalimo 145: 10 -12

10. Ntchito zanu zonse zidzakuyamikani, Yehova
    Ndi okondedwa anu adzakulemekezani.
11. Adzanenera ulemelero wa ufumu wanu,
    Adzalankhulira mphamvu yanu.
12. Kudziwitsa ana a anthu zamphamvu zache;
    Ndi ulemelero waukulu wa ufumu wache

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 6
KUITANIDWA KWA ABRAHAMU

1. **Ndi chifukwa chiyani Mulungu anamuitana Abrahamu kuchokera ku Ur mu Chaldea?**
   Kuti apitilize pangano lake ndi Abrahamu komanso mbeu yake mu dziko lolonjezedwalo. (Genesesi 12:1)

2. **Kodi izi zinachitika mwa pangano monga mmene Mulungu analankhulira kudzera mwa Nowa?**
   Inde, popeza Abrahamu anali mbumba ya Semu. (Genesesi:9:2; 11:11-25)

3. **Kodi anthu a ku Kana anali owopa Mulungu?**
   Iyayi, anali anthu oipa ochokera kwa Hamu. (Genesesi 10:1-20)

4. **Nanga ndi chifukwa chiyani Mulungu anatumiza Abrahamu ku dziko lotereli?**
   Chifukwa anali kufuna kuti akakhale mlendo m'dera lolonjezedwali. (Genesesi 12:6-7,10; onaninso Ahebri 11:8-10)

5. **Nanga ndi chifukwa chiyani Mulungu anafuna kuti Abrahamu akakhale mlendo mu dera lolonjezedwalo?**
   Chifukwa deralo linali loti likhale ngati lamuyaya lochokera kwa Khristu limene silidzakhala lakelake la Abrahamu kufikira kutha kwa nthawi ya dziko lapansi. (Ahebri 10:15-16)

6. **Kodi Abrahamu anaonetsa bwanji chikhulupiliro chake mu chipangano cha Mulungu?**
   Anakana kupalana ubwenzi ndi anthu oipa a ku Kana. (Ahebri 11:9)

7. **Kodi Abrahamu anaonetsa bwanji kuti sanali okhulupilira Mulungu nthawi zonse?**
   Ananena bodza lokhudza mkazi wake kawiri kuti adzipulumutse. (Genesesi 12:10-13; 20:1-2)

8. **Kodi Abrahamu anapatsidwa mwana molingana ndi lonjezano?**
   Inde, Mulungu anapatsa Abrahamu ndi Sarai mwana mu ukalamba wawo (Genesesi 21:1-5)

9. **Kodi Mulungu anapangiranji kuti Abrahamu adikire nthawi yaitali chomwechi kuti amupatse mwana?**
   Kuti awonetse kuti kubadwa kwa Isaki kunali chodabwitsa cha chisomo chake. (Aroma 9:6-9; Ahebri 11:11-12)

10. **Kodi Mulungu ananenanji zokhuzana ndi Isaki?**
    " Ndipo Mulungu anati kwa Abrahamu, Usaipidwe nawo chifukwa cha mnyamatayo, ndi chifukwa cha mdzakazi wako;momwe monse akunenera Sara umvere mau ache onse, chifukwa kuti mwa Isaki zidzaitanidwa mbeu zako." (Genesesi 21:12)

Ndime Zapamtima : Masalimo 145: 13 -16

13. Ufumu wanu ndiwo ufumu womka muyaya
    Ndi kuweruza kwanu kufikira mibadwo yanu yonse
14. Yehova agwiriziza onse akugwa, naongoletsa onse owerama.
15. Maso a onse oyembekeza inu
    Ndipo muwapatsa chakudya chanu m'nyengo zawo.
16. Muolowetsa dzanja lanu, Nimukwaniritsa zamoyo zonse chokhumba chawo.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 7
PANGANO MONGA MMENE CHINAKHADZIKITSIDWIRA NDI ABRAHAMU

1. **Kodi ndi udindo wanji umene Mulungu anapereka kwa Abrahamu mogwirizana ndi chipangano?**
   Mulungu anamupanga iye kukhala tate wa fuko lonse. (Aroma 4:12)

2. **Kodi ndi chiyani chomwe Mulungu anaonetsera kwa Abrahamu ngati tate wa okhulupirira onse**?
   Anamuuza kuti mbeu yake idzachuluka ngati mchenga wa ku nyanja. (Genesesi 22:17)

3. **Kodi mbeu imeneyi ndi iti?**
   Khristu ndi onse amene ali amodzi mu chikhulupiliro. (Agalatia 3:16; 1 Akorinto 3:23)

4. **Kodi Mulungu anayesa bwanji chikhulupiliro cha Abrahamu?**
   Mulungu anamuuza iye kuti apereke mwana wake yekhayo, Isaki ngati nsembe. (Genesesi 22:1-2)

5. **Kodi Abrahamu anaonetsa bwanji kukhulupilira kwake mu lonjezo la Mulungu?**
   Anakhulupilira kuti Mulungu atha kuukitsa Isaki kuchokera ku imfa. (Ahebri 11:17-19)

6. **Kodi Mulungu anaphunzitsa Abrahamu chiyani pomuyesa chikhulupiliro chake?**
   Anamuphunzitsa kuti Mulungu adzapereka Khristu ngati nkhosa yomwe idzalowe mmalo mwa anthu ake. (Genesesi 22:13-14; Yohane 1:29)

7. **Kodi ndi chizindikiro chanji chomwe Mulungu anapereka kwa Abrahamu ndi mbumba yake?**
   Chizindikiro cha mdulidwe womwe lero wasandulika ubatizo. (Genesesi 17:9-14)

8. **Kodi Sarai anakakamira bwanji kuti Isaki alandire mdalitso wachipangano?**
   Anauza Abraham kuti amuthamangitse Isimaeli. (Genesesi 21:9-10)

9. **Ndichifukwa chiyani Abraham anatumiza wantchito wake ku Haran kuti akamupezere Isaki mkazi?**
   Amafuna kuti Isaki akwatire mkazi woopa Mulungu. (Genesesi 24:3-4)

10. **Kodi Mulungu anaonetsera chiyani chomwe chidzachitikire mbeu ya Abraham asanalandire dziko lolonjezedwa?**
    Mulungu anauza Abraham kuti mbumba yake idzasautsidwa kwa zaka mazana anayi mu dziko lachilendo. (Genesesi 15:13)

Ndime zapamtima: Masalimo 145: 17-19

17. Yehova ali wolungama mnjira zake zonse.
    Ndi wachifundomuntchito zake zonse.
18. Yehova ali pafupi ndi onse akuitanira kwa iye;
    Onse akuitanira kwa iye muchoonadi.
19. Adzachita chokhumba iwo akumuopa; Nadzamva kufuula kwawo;
    Nadzawapulumutsa.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 8
ANTHU A M'CHIPANGANO ACHULUKANA

1. **Kodi ana onse obadwa mchipangano, ndi ana a pangano kapena osankhidwa a Mulungu?**
   Iyayi, Mulungu akutionetsa kudzera mwa ana a mapasa a Isaki ndi Rabeka kuti sanali otero. (Aroma 9:13)

2. **Kodi Mulungu ananena chiyani zokhuza ana awiri amapasa a Isaac pa Aroma 9:13?**
   " .Inde monga kunalembedwa, ndinakonda Yakobo ndipo ndinamuda Essau"

3. **Kodi Yakobo adatani kuti alandire mdalitso?**
   Ananamiza abambo ake popeza anali wosaona. (Genesesi 27)

4. **Kodi izi zinali zolakwika motani?**
   Chifukwa zinaonetsa kuti samakhulupilira Mulungu. (monga Masalimo 37:3)

5. **Kodi Essau anatani pamene Yakobo analandila mdalitso?**
   Anakonzekera kuti aphe Yakobo pamene bambo wake anamwalira. (Genesesi 27:41)

6. **Kodi Mulungu analonjeza chiyani kwa Yakobo mmaloto pamene anathawa ukali wa Essau?**
   Analonjeza kuti adzamusamala ku Harani komanso adzamubwezera ku dziko lalonjezano. (Genesesi 28:13-15)

7. **Kodi Mulungu anasunga bwanji panganoli kwa Yakobo?**
   Mulungu anamupatsa banja komanso chuma chochuluka. (Genesesi 30)

8. **Kodi Mulungu anamutsimikizira bwanji Yakobo za kupitilira kwa madalitso pamene anabwelera ku Kana?**
   Mulungu anauza Yakobo kuti lonjezolo lidzakwaniritsidwa kudzera mwa iye ndi ana ake. (Genesesi 28:13-15)

9. **Kodi Mulungu anamupatsa Yakobo ana angati?**
   Mulungu anamupatsa Yakobo ana khumi ndi awiri ndipo kuchokera mwa iwo mitundu khumi ndi iwiri ya Isalaeli inatchulidwa. (Genesesi 35: 22-26)

10. **Kodi ndi chiyani chomwe miyoyo ya ana a Yakobo yatiphunzitsa?**

Tiphunzira kuti Mulungu amaonetsa kukhulupilika kwake kwa iwo ngakhale anali ochimwa.

Ndime zapamtima: Masalimo 145:20-21

20. Yehova asunga onse akukondana naye;
    Koma oipa onse adzawaononga.
21. Pakamwa panga padzanena chilemekezo cha Yehova; Ndi zinthu zonse zilemekeze dzina
    Lake loyera ku nthawi za nthawi.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 9
ANTHU ACHIPANGANO MU UKAPOLO KU AIGUPUTO

1. **Kodi ndi chinthu chanji choipa chimene ana khumi a Yakobo anachita?**
   Anamugulitsa Yosefe ngati kapolo ku Aiguputo. (Genesesi 37: 27-32)

2. **Kodi Mulungu anafunira Yosefe choipa?**
   Iyayi, ngakhale abale ake anamufunira zoipa , Mulungu anamukonda iye namufunira zabwino. (Genesesi 50:20)

3. **Kodi Mulungu anawonetsa bwanji kumukondera kwake kwa Yosefe ku Aiguputo?**
   Mulungu anamusintha iye kuchoka mu ukapolo komanso kundende ndi kukhala olamulira ku Aiguputo. (Genesesi 41:39-44)

4. **Kodi ana khumi a Yakobo anawonetsa kusintha khalidwe lawo mtsogolo?**
   Inde, iwo anavomera kulakwa kwawo kwa Yosefe. (Genesesi 44:18 mpaka kutsogolo)

5. **Kodi Yakobo anatani atamva kuti Yosefe ali moyo?**
   Ndi mdalitso wa Mulungu Yakobo ndi banja lake anasamuka kupita ku Aiguputo. (Genesesi 46:1-7)

6. **Kodi Mulungu anatengeranji Yakobo ndi banja lake kupita nawo ku Aiguputo**?
   Mulungu anali kufuna kuonetsa ukulu wake powapulumutsa anthu ake ku ukapolo ndi nkhanza ya Aiguputo. (Genesesi 48:21; 50:24, Machitidwe a Atumwi 7:6-7)

7. **Kodi Mulungu anabweretsa bwanji nkhanza ndi ukapolo umenewu?**
   Mulungu anakuza mfumu ya nkhanza pakati pa Aiguputo imene inasandutsa ana a Israeli kukhala akapolo. (Exsodo 1:8-14)

8. **Kodi ukapolo umenewu utanthauza chiyani?**
   Ukapolowu ukutanthauza kuzunzika kwa mzimu chifukwa cha tchimo. (Luka 1:74-75; Levitiko 11: 44-45)

9. **Kodi ndi chiyani china chimene Mulungu anaphunzitsa ana ake kudzera mu ukapolowu?**
   Mulungu anawaphunzitsa kuti timalandira malonjezo ake a iye kudzera mu zozizwitsa za chisomo chake. (Genesesi 17:7; Aroma 3:29; 1 Petro 1:15-25)

10. **Kodi ndi chiyani chomwe chinawapatsa ana a Israeli chiyembekezo mu kuzunzika Kwawo?**
    Mulungu anawalonjeza kuti adzawapititsa kwawo ku Kanani. (Genesesi 15:13-14)

Ndime zapamtima: Masalimo 105: 1-3

1. Yamikani Yehova, itanirani pa dzina lake;
   Bukitsani mwa mitundu ya anthu zochita Iye.
2. Muyimbileni , muyimbileni zomulemekeza, fotokozerani zodabwiza zake zonse.
3. Mudzitamandile ndi dzina lake loyera. Mitima yawo ya iwo ofunsira Yehova ikondwere

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 10
KUWOMBOLEDWA PA NYANJA YAIKULU YOFIIRA

1. **Kodi Mulungu anamukonza ndani kuti akapulumutse anthu ake ku Aiguputo?**
   Mulungu anamusankha Mose kuti akagwire ntchitoyi. (Eksodo 2:3)

2. **Kodi Mulungu anamukonza bwanji Mose m'masiku oyamba a moyo wake?**
   Mulungu anakonza moyo wa Mose kuti athe kulandila chiphunzitso m'nyumba ya makolo ake. (Eksodo 2: 8-10)

3. **Kodi tidziwa bwanji zoti Mulungu amamukonzekeretsa Mose kudzera mmabwalo a chifumu ku Aiguputo?**
   Anaphunzira machitidwe ndi nzeru za Aiguputo zomwe zinamuthandiza kutsogolera anthu ake. (Machitidwe a atumwi 7:22)

4. **Kodi chiphunzitso china chomwe Mose analandira ndi chotani?**
   Iye anakhala zaka zisanu ali ku Midiani ngati m'busa wa ziweto. (Eksodo 3:1)

5. **Kodi Mulungu anamuitana bwanji Mose kuti akagwire ntchito yopulumutsa anthu ake?**
   Mulungu anamuyankhula kudzera mu chitsamba choyaka moto ndikumupatsanso zizindikiro zoti akamuonetse Farao. (Eksodo 3:1-10; 4: 1-9)

6. **Kodi Farao anali kufuna kuti awaleke ana a Israeli kuti apite?**
   Iyayi, Mulungu anaumitsa mtima wake ndi kuonetsa ukulu wake kudzera mwa iye. (Eksodo 7:4; Aroma 9:17-18)

7. **Kodi Mulungu anaonetsa bwanji mphamvu yake ku Aiguputo?**
   Mulungu anatumiza miliri khumi kuti Farao athe kuzindikira kuti iye ndiye Mulungu wamakamu. (Eksodo 3:14; 7:14 –12:30)

8. **Kodi Mulungu anamulamula Mose ndi ana a Israeli kuti achite chiyani pamene mliri womaliza umachitika?**
   Anawauza kuti asunge Pasaka. (Eksodo 12:1-28)

9. **Kodi Pasaka imaimira chiyani?**
   Imaimira masautso komanso kukhetsa mwazi kwa Yesu pa mtanda. (1 Akorinto 5:7-8; 1 Petro 1:18-23)

10. **Kodi kufunikira kwa chiombolo cha pa nyanja yaikulu yofiira ndi kotani?**
    Kumasonyeza kuwomboledwa kwachiwiri kumene Mulungu anachitira mpingo wake.

Ndime zapamtima: Masalimo 105:4

4. Funani Yehova, ndi mphamvu yache
   Funsirani nkhope yake nthawi zonse.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

NTHAWI YACHITATU
ULENDO WA A ISRAELI KUBWERERA KU KANA MU NTHAWI YOMWE SOLOMO ANALI MFUMU YAWO.

PHUNZIRO 11
KUGALUKIRA KWA ANA A ISRAELI MCHIPULULU

1. **Kodi chomwe chinaonekera poyera pa ulendo wa ana a Israeli mchipululu ndi chiyani?**
   Zinaonekeratu kuti anali anthu ogalukira (mwachitsanzo Numeri 20: 1-5; 21:5)

2. **Kodi a Israeli anawonetsa bwanji kuti anali ogalukira?**
   Anatsutsana ndi Mose komanso Aroni nanena kuti anawatenga iwo kuchoka ku Aiguputo kuti adzafe ndi njala mchipululu. (mwachitsanzo Eksodo 16:1-3; 17:3)

3. **Kodi analankhuliranji chomwechi kwa Mose ndi Aroni?**
   Chifukwa anali ankhuli ndi chakudya cha ku Aiguputo ndipo sanakhulupilire kuti Mulungu angawapulumutse iwo ndi kuwapatsa zosowa zawo. (mwachitsanzo Eksodo 16:3; Numeri 11: 1-6)

4. **Kodi ndi tchimo lanji limene a Israeli anachita pa Meriba?**
   Iwo anakamba motsutsana ndi Mose ndipo anamuyesa Mulungu chifukwa panalibe madzi. (Eksodo 17:1-7)

5. **Kodi Mulungu anawonetsa bwanji kukhulupilika kwake?**
   Anawapatsa iwo mana kuchokera kumwamba ndiponso madzi kuchokera mu thanthwe. (Eksodo 16:14-15; 17:6-7)

6. **Kodi ndi kupambana kotani kumene Mulungu anawapatsa ana a Israeli pa Refidimu?**
   Aisraeli anagonjetsa a Amaleki pamene Mose anakweza manja ake kumwamba. (Eksodo 17: 8-16)

7. **Kodi ndi tchimo lanji lalikulu lomwe a Israeli analichita pa Sinai?**
   Iwo anapanga fano la golide nayamba kulilambira. (Eksodo 32)

8. **Kodi tchimo limeneli linadzetsa chiyani pakati pawo?**
   Tchimo lolambira mafano. (Machitidwe 7:38-43)

9. **Kodi Mulungu anaononga Israeli chifukwa cha tchimoli panthawiyi?**
   Iyayi, anawasiya iwo kuti adzakhale mphukira wa mbwadwo wina. (Eksodo 32:30 – 33:11 mpaka mtsogolo)

10. **Kodi Mulungu akutionetsa chiyani pa mbiriyi?**
    Akutionetsa kuti timapulumutsidwa kudzera mu chisomo osati ntchito zathu. (Aefeso 2:8-9)

Ndime zapamtima : Masalimo 105: 5-6

5. Kumbukirani zodabwitsa zake zimene anazichita;
   Zizindikilo zake ndi maweruzo a pakamwa pache.
6. Inu mbeu za Abrahamu, mtumiki wache.
   Inu ana a Yakobo, osankhika ake.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 12
ISRAELI ALANDIRA MALAMULO

1. **Kodi Mulungu anawapititsiranji ana a Israeli ku phiri la Sinai?**
   Kuti akakonzenso moyo wawo monga anthu ake a chipangano. (Eksodo 21 – 23:26; Ahebri 9)

2. **Kodi Mulungu anawapatsa chiyani ana a Israeli pa phiri la Sinai?**
   Anawapatsa iwo malamulo khumi komanso malamulo a zina ndi zina za makhalidwe awo. (Deutro 10:4)

3. **Kodi Mulungu akutiuza ife kuti tichite chiyani kudzera mmalamulo khumi amenewa?**
   Akutiuza kuti, " tikonde Mulungu ndi mtima wathu wonse, mphamvu zathu ndi zonse zathu komanso tikonde amnzathu monga tidzikondera ife eni" (Mariko 12: 30-31; Katekisimu Wachidule wa Westminister F42)

4. **Kodi lamulo likutiuza chiyani zokhudza ife eni?**
   Likutiuza kuti monga mwachilengedwe, titha kusakonda Mulungu komanso amnzathu. (Aroma 7:7; Agalatiya 5:19-21)

5. **Kodi Mulungu anagwiritsa bwanji ntchito lamulo kuti aphunzitse a Israeli za chipulumutso chawo?**
   Kudzera mu lamulo, Mulungu akuuza Israeli kuti akhale odikira kubwera kwa Khristu. (Agalatiya 3:24)

6. **Kodi ndi chiyani china chimene Mulungu anapereka kwa ana a Israeli kupatula Malamulo khumi aja?**
   Mulungu anawapatsa iwo mamangidwe a likasa komanso zoyenera kukhalamo. (Eksodo 25 – 27:21)

7. **Kodi likasa la Yehova ligwirizana bwanji ndi Khristu?**
   Likasalo pa lokha ndilo Khrisu amene adzakhala pakati pa anthu monga Mulungu – munthu, pamene nsembe zoperekedwa mu likasamo ndizo ntchito za Khristu amene anafera machimo athu (Yohane 1:14; Ahebri 8 – 10)

8. **Kodi Likasali limatchedwa nyumba ya Yehova chifukwa chiyani?**
   Chifukwa awa ndiwo anali malo amene Khristu amakhala ndi anthu ake. (Eksodo 25:22)

9. **Kodi Mulungu amakhala bwanji ndi anthu ake mu Likasamu?**
   Iye anali mu chifunga cha ulemelero mmalo oyera opezeka mu likasamo. (Eksodo 40:34)

10. **Kodi zinaonekeratu kuti Israeli sanali oyenera kukhala ndi Mulungu pakati pawo?**
    Inde, popeza Israeli anali kulambira fano la golide pamene Mose anatsikira kuchokera m'phiri. (Eksodo 32)

Ndime zapamtima: Masalimo 105: 7-8

7. Iye ndiye Yehova, Mulungu wathu
   Maweruzo ache akhala pa dziko lonse lapansi
8. Akumbukira chipangano chake kosatha
   Mauwo anawalamulira mibadwo zikwi.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 13
MPINGO WA KHRISTU MCHIPULULU

1. **Kodi chimene chinapangitsa kukhala posinthila zinthu pa ulendo wa ana a Israel ndi chiyani?**
   Israeli sanali ololedwa kulowa mu kanani chifukwa cha kusakhulupilira kwake mwa Mulungu. (Numeri 13; 14)

2. **Kodi anasonyeza bwanji kusakhulupilika kwawo?**
   Iwo anakana kumvera zonena za Yoswa komanso Kalebe ndikumvera zomwe akazitape khumi ochimwawo anawauza iwo. (Numeri 14: 1-4,10)

3. **Kodi izi zinaonetsa bwanji kusakhulupilira kwawo?**
   Chifukwa sanakhulupilire kuti Mulungu adzasunga pangano lake ndi kuwapatsa iwo malo olonjezedwawo. (Numeri 13: 30-33; 14:5-9)

4. **Kodi Mulungu anawalanga bwanji chifukwa cha kusakhulupiliraku?**
   Iye anapangitsa Israeli kuti azingoyendabe ndi kukhala mchipululu kwa zaka makumi anayi. (Masalimo 95:10; Numeri 14:33)

5. **Kodi chinachitika ndi chiyani mu zaka zimenezi?**
   Anthu onse oposera zaka makumi awiri kupatula Yoswa ndi Kalebe anafera mchipululu. (Numeri 14:19-39)

6. **Kodi zomwe zimachitika nthawi imeneyi zinali zotani?**
   Inali nthawi yomwe a Israeli anali kung'ung'udza komanso kugalukira. (Masalimo 95:10)

7. **Tchulani zitsanzo ziwiri za kugalukira kwa Israeli motsutsana ndi Mulungu wawo?**
   Kugalukira kwa Kora, Dathan komanso Abiram motsutsana ndi Mose komanso Aroni; Kwachiwiri ndi kwa anthu ena onse ponyoza mana amene Mulungu anawapatsa komanso pakunena kuti anawatengera mchipululu kuti adzafe. (Numeri 16; 21:4-9)

8. **Kodi Mulungu anawalanga bwanji ana a Israeli pamene ananyoza manna amene Mulungu anawapatsa?**
   Anawatumizira njoka zolusa zomwe zinapha ambiri a iwo. (Numeri 21: 8-9)

9. **Kodi Mulungu anawapulumutsa bwanji ku njoka zimenezi?**
   Anamuuza Mose kuti ayike njoka yamkuwa ku ndodo ndipo onse oiwona iyo anapulumuka. (Numeri 21: 8-9)

10. **Kodi njoka yamkuwa isonyeza chiyani?**
    Isonyeza za Yesu Khristu amene anena kuti," ndipo monga Mose anakweza njoka mchipululu, chotero mwana wamunthu ayenera kukwezedwa kuti yense wokhulupilira iye akhale nawo moyo wosatha" (Yohane 3:14-15)

Ndime zapamtima: Masalimo 105: 9-10

9. Chipanganocho anapangana ndi Abrahamu, ndi lumbilo lake ndi Isaki
10. Ndipo anachiimikira Yakobo chikhale malemba, chikhale chipangano
    Chosatha kwa a Israeli.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 14
ANA A ISRAELI ALOWA MU DZIKO LALONJEZANO

1. **Kodi Mulungu anamuletseranji Mose kuti asakalowe nawo mu dziko lalonjezanolo?**
   Popeza mu mkwiyo wake ndi ana a Israeli, Mose anamenya thanthwe. (Numeri 20:1-13)

2. **Kodi zimene Mose anachitazi zitionetsa chiyani?**
   Zitidziwitsa kuti iye anali nkhalapakati chabe, kotero, wosalungama. (Numeri 20:12; 27:14; Masalimo 106:32-33)

3. **Kodi ndi ndani amene Mose anali nkhalapakati wake?**
   Khristu amene ali nkhalapakati wa chipangano chabwino. (Ahebri 8:6)

4. **Kodi ndi ndani amene Mulungu anamuitana kuti atsogolere Israeli polowa mu Kanani?**
   Yoswa amene anali ngati mmodzi wa Khristu. (Yoswa 1:1-2)

5. **Kodi Mulungu anasonyeza bwanji kuti anatsegulira njira ya ku Kanani?**
   Pogawa madzi a mu Yorodano kwa iwo. (Yoswa 3)

6. **Kodi ndi mbali iti ya yorodano imene Israeli anagonjetsa koyambilira?**
   Gawo lapakati kuyambira ndi Yeriko. (Yoswa 6)

7. **Kodi Mulungu akutidziwitsa chiyani pa zakupulumutsidwa kwa Rahabi ndi abale ake?**
   Atiphunzitsa kuti Mulungu adzasankha anthu ake ngakhale kuchokera kwa anthu amene sali Ayuda. (Masalimo 87:1-5)

8. **Kodi kupulumutsidwa kwa Rahabi kudali molingana ndi lonjezo la Mulungu kwa Abrahamu?**
   Inde, pakuti Mulungu anati , “m'mbeu yako mtundu wonse wadziko lapansi udzadalitsika” (Genesesi 22:18)

9. **Kodi Israeli anagonjetsa bwanji dera la kuzambwe kwa Yorodano?**
   Poyamba, dera la ku phiri cha kum'mawa kenaka dera lamapiri la kumadzulo. (Yoswa 11:16-17)

10. **Kodi dera limeneli linagawidwa bwanji kwa mitundu yonse khumi ndi iwiri ya Israeli?**
Mulungu anagawa malowa pochita maere (Yoswa 13:1-8; 14:1-5)

Ndime zapamtima: Masalimo 105: 11-13

11. Ndikunena kuti ndidzakupatsa iwe dziko la Kanani, Gawo la cholandila chako.
12. Pokhala iwo anthu owerengeka,Inde, anthu pang’ono, ndi alendo m’mwemo.
13. Nayendayenda kuchokera mtundu wina kufikira mtundu wina.
    Kuchokera ufumu wina kufikira anthu ena.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 15
KUCHIMWA KWA ISRAELI M'DZIKO LALONJEZANO

1. **Kodi Israeli anakhalabe okhulupirika kwa Mulungu m'dziko lalonjezano?**
   Ayi, ananyoza Mulungu nayambanso kulambira mafano. (Oweruza 2:11-13)

2. **Kodi chinapangitsa izi chinali chiyani?**
   Makolo sanalangize ana awo kuti akule moopa Mulungu. (Oweruza 2:10)

3. **Kodi Israeli anagonjetsa maiko achikunja omwe anawapeza mu kanani monga mmene Yehova ananenera?**
   Iyayi, sanamvere zimene Mulungu anawalonjeza ndipo anapalana maubwenzi ndi amitundu enawa. (Oweruza 2:1-2)

4. **Kodi Mulungu anawachita chiyani ana a Israeli pazimene anachita zopalana ubwenzi ndi adani ake?**
   Mulungu anawapatsa mphamvu adaniwo ndikulola kuti Israeli akhale mu ulamuliro wawo. (Oweruza 2; 3)

5. **Kodi Mulungu anawakumbukira iwo mu nthawi yawo ya mtsautso?**
   Inde, anawatumizira oweruza kuti akawaombole pamene analapa za kuchimwa kwawo. (Oweruza 2:16-18)

6. **Kodi Yehova anapereka phunziro lanji kudzera mu kupambana kwa Gideoni ndi ankhondo ake ochepa?**
   Aphunzitsa kuti kupambana kumachokera kwa Mulungu nthawi zonse. (Oweruza 7:1-7)

7. **Pamene uthenga wa Mulungu unali wochepa mu Israeli, Kodi ndi ndani amene Mulungu analankhula kudzera mwa iye?**
   Kudzera mwa Samueli amene anali mneneri komanso wansembe. (1 Samueli 3:19 – 4:1)

8. **Kodi ndi chiyani choipa chimene ana a Israeli anapempha?**
   Anamupempha Samueli kuti awapatse mfumu monga mmene zinaliri ndi maiko ena. (1 Samueli 8)

9. **Kodi ndi chifukwa chiyani Pempholi linali lolakwika?**
   Chifukwa popanga izi, amasonyeza kukana Mulungu kukhala mfumu yawo. (1 Samueli 8:7)

10. **Kodi nthawi ya oweruzayi imadziwika ndi chiyani?**
    Munthu aliyense anali kuchita zomwe zimamukomera. (Oweruza 21:25)

Ndime zapamtima: Masalimo105: 14-15

14. Sanalola munthu awatsutse;
    Ndipo anadzudzula mafumu chifukwa cha iwowa.
15. Ndi kuti musamakhudza ozozedwa anga;
    Musamachitira choipa aneneri anga.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 16
ISRAELI ALANDILA DZIKO LONSE LALONJEZANO

1. **Kodi Mulungu anapatsa a Israeli mfumu monga mmene anafunira?**
   Inde, anawapatsa iwo Sauli kuti akhale mfumu yawo. (1 Samueli 10)

2. **Ndi ndani amene Mulungu anawapatsa mmalo mwa Sauli pamene anachimwira Yehova?**
   Anasankha Davide kukhala mfumu yawo. (1 Samueli 16)

3. **Kodi Mulungu anawapatsa chiyani a Israeli kudzera mwa Davide?**
   Kudzera mwa Davide, Mulungu anawapatsa iwo dziko lalonjezano monga mmene anamuuzira Abraham. (Genesesi 15: 18-21)

4. **Kodi ndi chifukwa chiyani Davide sanamange nyumba ya Yehova Yehova?**
   Chifukwa anali wokangalika ndi kumenya nkhondo zambiri. (1 Mbiri 22:8)

5. **Kodi ndi chiyani chomwe Mulungu anapereka kwa Davide chokhudzana ndi kumanga kwa nyumba ya Yehova?**
   Iye anamuuza Davide kuti adzamupatsa mwana wamwamuna amene adzamange nyumba ya Yehova (2 Sam.7:12-13)

6. **Kodi ndi kufunikira kwanji kumene nyumba ya Yehova kunali nako pakati pa Israeli?**
   Ndiye pamene panali likulu la ulamuliro wa Mulungu (Theocracy). (Deut 12:13; Onaninso 1 mbiri 22:6-19)

7. **Kodi zinatheka bwanji kuti nyumbayi ikhale likulu la ulamuliro wa Mulunguwu?**
   Chifukwa Mulungu anaisankha nyumbayi kuti isonyeze kupezeka kwake pakati pa anthu ake. (1 Mbiri 22:19; Eksodo 25:22)

8. **Kodi ulamuliro wa Solomo unadziwika ndi chiyani?**
   Inali nthawi ya mtendere komanso imene zinthu zinapita patsogolo. (1 Mafumu 4:21-25; 1 Mbiri 2:9)

9. **Kodi kupambana kwa Davide kunali kosonyeza chiyani?**
   Kusonyeza kupambana kwa Ambuye Yesu kwa anthu ake pa tchimo , satana komanso dziko lapansi lankhanzalo. (Luka 1: 74-75; onaninso Masalimo 56; 72:1-9 ndi ena)

10. **Kodi ulamuliro wa Solomo wamtendere ndi kutukuka kusonyeza chiyani?**
    Kusonyeza kukoma ndi ulemelero wa ufumu wa Khristu umene uli nkudza. (1 Mafumu 4: 21-25; onaninso Yesaya 9:6-7; 11:6-9; Chivumbulutso 12:10-11; Aefeso 2:14-17 ndi ena)

Ndime zapamtima : Masalimo 45: 1-2

1. Mtima wanga usefukira nacho chinthu chokoma; ndinena zopeka ine zamfumu
   Lirime langa ndilo peni yofulumira kulemba
2. Inu ndinu wokongola ndithu koposa ana a anthu;
   Anakutsanulirani chisomo pa milomo yanu, Chifukwa chake Mulungu anakudalitsani kosatha.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

NTHAWI YACHINAYI
KUGAWIKANA KWA MAUFUMU KUFIKIRA KUBWELERA KUCHOKERA KU UKAPOLO

PHUNZIRO 17
KUGAWIKANA KWA UFUMU

1. **Kodi ufumu wa Solomo unali ngati kukwaniritsa kwa lonjezo la Mulungu kwa Abraham?**
   Inde, kunali kukwaniritsa kwa lonjezoli. (Onani Genesesi 17:6-8)

2. **Kodi choonadi chimene izi zinalosera chinali chotani?**
   Umuyaya wa ufumu wa Khristu mu Kanani wakumwamba. (Ahebri 11:8-10, 13-16 Chivumbulutso 5:6-14 ndi ena)

3. **Kodi Mulungu anamulanga bwanji Solomo chifukwa cha kulambira kwake kwa mafano?**
   Analanda mitundu khumi kuchokera ku nyumba ya Davide naipereka kwa Jeroboamu. (1 Mafumu 11:35)

4. **Kodi chinachitika ndi chiyani kuti anthuwa agawikane?**
   Rehoboam anakana kusitsa misonkho yomwe anthu amapereka pamene nyumba yachifumu komanso ya Yehova zinamangidwa. (1 Mafumu 12: 3-5, 12-14)

5. **Kodi ndi chifukwa chiyani linali tchimo kuti mitundu khumi ichoke kunyumba ya Davide?**
   Pakuti potero anamukana Khristu amene Yehova anamusankha kuti akhale pa ufumu wa Davide. (1 Mafumu 12:16, 19, 25-29; onaninso Yesaya 9:6-7)

6. **Kodi ndi mdalitso wina wotani umene ufumu wa Yuda unali nawo kupatula kukhala wa Fuko la Davide?**
   Ufumu wa Yuda unali ndi nyumba ya Yehova mu Yerusalemu. (1 Mafumu 12: 26-27)

7. **Kodi ndi mitundu iwiri iti amene Yehova anasiyira Rehoboam kuti awalamulire?**
   Mitundu ya Yuda ndi Benjameni. (2 Mbiri 11:1-2)

8. **Kodi Rehoboamu anakakamiza mitunduyi kuti imuvomereze kukhala mfumu yawo?**
   Inde, koma Mulungu sanamulole kuti amenyane nkhondo ndi abale ake.(1 Mafumu 12: 23-24)

9. **Kodi munganene chiyani za maufumu a Yuda?**
   Onse anali ochokera ku nyumba ya Davide. (monga 1 Mafumu 11:43; 14:31; 15:8; 22:41; 2 Mafumu 8:16 ndi ena)

10. **Ndichifukwa chiyani maufumu onsewa anali ochokera kunyumba ya Davide?**
    Chifukwa Mulungu analonjeza kudzakhazikitsa ufumu wa Davide kwa muyaya. (2 Samueli 7:16-17; onaninso Yesaya 9:6-7)

Ndime zapamtima: Masalimo 45: 3-4

3. Dzimangireni lupanga lanu mchiuno mwanu mwamphamvu inu;
   Ndi ulemelero wanu ndi ukulu wanu.
4. Ndipo pindulani mu ukulu wanu yendani;
   Kaamba ka choonadi ndi chifatso ndi chilungamo: Ndipo dzanja lanu lidzakuphunzitsani zoopsa.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 18
UFUMU WA ISRAELI UYAMBA KULAMBIRA MAFANO

1. **Kodi malemba amakamba chiyani za Yeroboamu , mfumu yoyamba ya mitundu khumi ija?**
   Amatchedwa “Yeroboamu..zimene zinapangitsa Israeli kuchimwa” (2 Mafumu 13:2)

2. **Nchifukwa chiyani amatchedwa Yeroboamu amene anapangitsa Israeli wa ku mpoto kuti achimwe?**
   Chifukwa analamula Israeli kuti ayambe kulambira zosema zonga ng'ombe za golide. (mwachitsanzo 1 Mafumu 12:28-29, 2 Mafumu 17:21)

3. **Kodi zimenezi zinamupangitsa Israeli kuchita tchimo lanji?**
   Israeli anayamba kulambira mafano onse a mayiko a chikunja a mu Kanani. (mwachitsanzo 2 Mafumu 17:7-12)

4. **Kodi ndi fano lanji limene Israeli amalambira?**
   Mu nthawi ya mfumu Ahabu, Israeli anali kulambira Baala. (1 Mafumu 16: 30-33)

5. **Kodi inalipo mphukira yomwe inakhalabe yokhulupilira Mulungu mu nthawi ya Ahabu?**
   Inde, analipo anthu okwana zikwi zisanu ndi ziwiri (7000) amene anakana kugwadira Baala. (1 Mafumu 19:18)

6. **Kodi ndi ndani amene Mulungu anamutumiza kuti akatsutsane ndi kulambira mafanoku?**
   Anatuma mneneri Eliya komanso Elisa amene anafalitsa uthenga wakuti Yehova ndiye Mulungu woona. (mwachitsanzo monga 2 Mafumu 2:13-14; Aroma 11:2-4)

7. **Kodi ndi aneneri ati amene amamuchenjeza Israeli za chigamulo cha Mulungu chimene chiri nkuza?**
   Aneneri otchedwa Amosi komanso Hosea. (monga Hosea 1: 1-2; 4:1 mpaka mtsogolo; Amos 1:1-2; 3:1-2)

8. **Ndi nthawi iti imene mphukira yosankhikayo inaonetsa chikhulupiliro chake?**
   Pamene anabwelera ku Yerusalemu kukachita pasaka munthawi yomwe Hezekiya anali mfumu ya yuda. (2 Mbiri 30:10-11)

9. **Kodi Mulungu anawalanga bwanji a mitundu khumi akumpotowo pa za kuchimwa kwawo?**
   Mulungu anatumiza a Assyria kuti adzawagwire ukapolo ndikuwabalalitsa. (2 Mafumu 17)

10. **Kodi ndi ndani amene mfumu ya Assyria inawaika mmalo mwawo?**
    Anaikamo anthu a ku Samariya amene anali achilendo otengedwa ku mbali zosiyanasiyana za ku Assyria. (2 Mafumu 17:24)

Ndime zapamtima: Masalimo 45: 5-6

5. Mivi yanu njakuthwa;
   Mitundu ya anthu igwa pansi pa inu, iwalasa mumtima adani a mfumu.
6. Mpando wachifumu wanu, Mulungu, ukhala nthawi zonse zomka muyaya
   Ndodo yachifumu ya ufumu wanu ndiyo yolunjika.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 19
UFUMU WA YUDA ULEKANA NDI MULUNGU

1. **Kodi ufumu wa Yuda unali wochepera kwa ufumu wa Israeli?**
   Inde, anthu okhulupilira amakhala ochepa kusiyana ndi ochimwa. (onaninso monga 1 Mafumu 12:21-24; 2 Mafumu 19: 1-4)

2. **Kodi analipo mu Yudea anthu amene anali kulambira mafano?**
   Inde, uchimo unakhazikika mu dera la Yuda. (1 Mafumu 14:22-24)

3. **Kodi mafumu onse a Yuda anali owopa Mulungu?**
   Iyayi, ambiri a iwo anamulowetsa Yuda mukulambira mafano. (mwachitsanzo 2 Mafumu 8:18-19, 27; 11:1-3; 16:2-4)

4. **Kodi ndi chinthu chanji choipa chimene mfumukazi Ataliah anafuna kuchita?**
   Anayesetsa kuti aphe mbeu yachifumu ya Davide. (2 Mbiri 22: 1-12)

5. **Kodi ndi chifukwa chiyani satana anafuna kupha mbeu ya Davideyi kudzera mwa mfumukazi Ataliah?**
   Chifukwa kunalembedwa kuti Khristu adzabadwa kuchokera ku mbeu ya Davide. (1 Mafumu 9:5; 2 Mbiri 13:5; Yesaya 9:6-7)

6. **Kodi Mulungu anasunga bwanji mbeuyi kuti ikhale ndi moyo?**
   Anamusunga ndi moyo mwana wa khanda wotchedwa Joasi kuti asaphedwe ndi Ataliah woipayo. (2 Mafumu 11:1-2)

7. **Kodi ndi mafumu ati amene anadziwika chifukwa cha kukhulupilira komanso chiyero chawo?**
   Asa, Yoasi, Hezekiya komanso Yosaya amene anathetsa kupembedza kwa mafano, kukhadzikitsanso nyumba ya Yehova ndikuuza Yuda kuti adzikumbukira pasaka. (1 Mafumu 15: 9-15; 2 Mbiri 24:1-4; 1 Mafumu 22:42-43; 2 Mbiri 30:1-2; 2 Mafumu 22:1-2 ; 23:19-25; ndi ena)

8. **Kodi ndi aneneri ati amene Mulungu anawakuza kuti aphunzitse Yuda za iye?**
   Yesaya komanso Yeremiya amene kudzera mwa iwo Mulungu ananeneratu za ukapolo wa Yuda komanso kubwerera kwa mphukira yake. (Yesaya 1; Yeremiya 1:1-2; 3:23 – 4:6 ndi ena)

9. **Kodi Mulungu analankhula za Khristu kwa Yuda mmasiku amenewa?**
   Inde, kudzera mwa mneneri Mika analankhuliratu za Betelehemu kukhala malo amene Yesu adzabadwire. (Mika 5:2)

10. **Kodi Yuda anasinthika kuchoka ku njira zake zoipa?**
    Ayi, anachimwirachimwirabe monga mmene Israeli anachitira. (monga 2 Mafumu 23: 26-27; 24:3-9)

Ndime zapamtima: Masalimo 45: 7-8

7. Mukonda chilungamo ndipo mudana nacho choipa
   Chifukwa chake Mulungu, ndiye Mulungu wanu, wadzodza inu ndi mafuta
   A chikondwelero koposa amnzanu.
8. Zobvala zanu zonse ndi za mure, ndi khonje ndi kasya:
   Mzinyumba zamfumu zomanga ndi minyanga ya njovu mwaturuka
   Zoyimba zazingwe zokukondweretsani.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 20
YUDA AGWIDWA UKAPOLO

1. **Kodi Mulungu analanga bwanji kuchimwa kwa Yuda?**
   Mulungu anatumiza Nebuchadnezzar kuti adzagwire Yuda ukapolo. (2 Mbiri 36)

2. **Kodi anthu ake a Mulungu anatengedwa nawo kupita ku ukapoloko?**
   Inde, mwachitsanzo, Danieli ndi amnzake atatu. (Danieli 1:1-4, 6-7)

3. **Kodi Nebuchadnezzar anawatengera kuti akapolowa?**
   Anapita nawo ku Babulo. (Yeremiya 53: 28-32)

4. **Kodi Mulungu sanalonjeze ana a Israeli kuti adzawapatsa Kanani kukhala dziko lawo?**
   Inde, koma lonjezoli likukwaniritsidwa pamene osankhikawo adzapatsidwa dziko laulemelero. (Chivumbulutso 21 – 22:7)

5. **Kodi a mafukowo anazindikira kuti lonjezoli limanena ulemelero wa kumwamba?**
   Inde, popeza iwo anali ofunika kuwapatsa dziko la ulemelero wa Yehova. (Ahebri 11:10, 13-16)

6. **Kodi chimene chinachitikira nyumba ya Yehova komanso ufumu wa Davide ku Yerusalemu chinali chiyani?**
   Zonse zinawononongedwa ndipo mzinda wonse unaotchedwa. (2 Mafumu 25: 8-9,17)

7. **Kodi Mulungu anafuniranji kuti izi zionongedwe?**
   Chifukwa anafuna kuti anthu ake aphunzire kufunafuna ufumu wa Khristu mu Yerusalemu watsopano. (Chivumbulutso 3:11-13)

8. **Kodi kugwidwa kwa ukapoloku kunawapangitsa chiyani anthu ake a Mulungu okhulupilira?**
   Iwo anayamba kufunitsitsa nyumba ya ufumu wake wa Mulungu. (Masalimo 137)

9. **Kodi Danieli anasonyeza bwanji chikhulupiliro chake mwa Mulungu pamene anali ku Babulo?**
   Iye anali kupemphera moyang'ana ku Yerusalemu kumene kunali nyumba ya Yehova. (Danieli 6:10)

10. **Kodi ndani amene analimbikitsa anthuwo kuti ayembekezere kubwerera kwawo ku Yerusalemu?**
    Mneneri Ezekieli amene anali mmodzi mwa akapolo pa mtsinje wa Chebara. (Ezekieli 1)

Ndime zapamtima: Masalimo 67: 1-4a

1. Atichitire chifundo Mulungu ndi kutidalitsa
   Atiwalitsire nkhope yache.
2. Kuti njira yanu idziwike dziko lapansi, chipulumutso chanu mwa amitundu onse.
3. Anthu akuyamikeni, Mulungu;
   Anthu onse akuyamikeni.
4. Anthu akondwere, nafuule mokondwera;

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 21
CHIFUNDO CHA MULUNGU PA OGWIDWA UKAPOLOWO

1. **Kodi ndi ulosi wanji umene unalembedwa mu nthawi ya ukapolo?**
   Buku la Danieli lomwe limakamba za kubwera kwa ufumu wa Khristu.

2. **Kodi Mulungu anaonetsa bwanji kubwera kwa ufumuwu kwa Nebuchadnezzar?**
   Kudzera mu loto la fano lalikulu lomwe linaonongedwa. (Dan 2)

3. **Kodi fanoli likuimira chiyani?**
   Maufumu a dziko lapansi amene Nebuchadnezzar anali mkulu wake. (Danieli 2:37-43)

4. **Kodi fano limeneli linaonongedwa bwanji?**
   Linaonongedwa ndi mwala omwe ukuimira ufumu wa Khristu. (Danieli 2:44-45)

5. **Kodi amnzake a Danieli atatu aja anazunzika chifukwa cha chikhulupiliro chawo?**
   Inde, anaponyedwa mu ng'anjo ya moto chifukwa anakana kulambira fano lomwe Nebuchadnezzar analipanga. (Danieli 3)

6. **Kodi Mulungu anawateteza bwanji anthu amenewa?**
   Anatumiza m'ngelo wake amene anayenda nawo mu ng'anjomo. (Danieli 3:24-28)

7. **Kodi Mulungu anawululira bwanji Belisezala za kugwa kwa Babulo?**
   Kudzera mu dzanja lomwe linalemba pakhoma ndipo Danieli anamasulira izi. (Danieli 5)

8. **Kodi Danieli anatetezedwa bwanji kwa adani ake?**
   Mulungu anateteza moyo wake mu dzenje lamikango. (Danieli 6)

9. **Kodi Mulungu anawaombola bwanji anthu ake ku ukapolo?**
   Patatha zaka makumi asanu ndi awiri, Mulungu anamupangitsa mfumu Sila kuti athe kulora anthuwo kuti apite. (Ezra 1:1-2)

10. **Kodi ayuda onse anabwelera kuchoka ku ukapolo?**
    Iyayi, ayuda ambiri anakondwera kuti atsalire ku Babulo. (monga Estere 2:5-7; 3:6)

Ndime zapamtima: Masalimo 67: 4b-7

4. Pakuti mudzaweruza anthu molunjika,
   Ndipo mudzalangiza anthu pa dziko lapansi.
5. Anthu akuyamikeni , Mulungu; Anthu onse akuyamikeni
6. Dziko lapansi lapereka zipatso zake, Mulungu, Mulungu wathu adzatidalitsa.
7. Mulungu adzatidalitsa;
   Ndipo malekezero onse a dziko lapansi adzamuopa iye.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 22
ISRAELI ABWELERA KU KANANI

1. **Kodi pamene anthuwo amabwelera ku Yerusalemu , anapeza mzinda wawo uli bwanji?**
   Anapeza Yerusalemu komanso nyumba ya Yehova zitasanduka bwinja. (Nehemiya 2:12-18)

2. **Kodi Mulungu anawalamuliranji kuti amangenso nyumba yake?**
   Chifukwa nyumbayi imasonyeza kupezeka kwake kwa Mulungu pakati pa anthu ake. (Ezra 1:1-5; 1 Mbiri 22:19; Eksodo 25:22)

3. **Kodi ndi chifukwa chiyani sitimapembedza mu kachisi ngati ameneyu masiku ano?**
   Chifukwa Khristu ndiye kachisi wa Yehova ndipo amakhala mmitima mwathu mwa uzimu wake. (Chivumbulutso 21:22; Aefeso 2:22)

4. **Ndani amene anali kuletsa Ayuda mmene amamanga nyumba ya Mulungu komanso Yerusalemu?**
   Anthu a ku Samariya komanso ena osakhulupilira amene anatsala ku Yerusalemu. (Ezara 4)

5. **Kodi amachitiranji izi?**
   Chifukwa anali kudana ndi Mulungu komanso anthu ake. (monga Nehemiya 2:19-20; 4:1-8)

6. **Kodi Ayudawa anatha kumanga nyumbayi?**
   Inde, popeza mfumu Dariyo analamula amene anali mkulu wa deralo kuti awaleke anthuwo kuti amange nyumbayo ndiponso kuti awapatse zimene zimafunika pomanga nyumbayo. (Ezara 6)

7. **Kodi anthuwo anachita chiyani pamene maziko a nyumbayo anakhadzikitsidwa?**
   Anthuwo anakuwa nayimba nyimbo zothokoza Chauta. (Ezara 3:11)

8. **Kodi ndi anthu onse amene anali wosangalala pamene nyumbayi inamangidwa?**
   Iyayi, amene anaona kukungola kwa Kachisi woyamba analira (Ezara 3:12)

9. **Kodi ufumu wa Davide unakhadzikitsidwanso?**
   Ngakhale panalibe wokhala pa mpando wachifumu wa Davide, mtundu wake unapitilira kukhala wachifumu. (Yeremiya 36:29-30; Yesaya 9:6-7)

10. **Kodi kufunikira kwa kubwereranso kwa anthu ake a Mulungu ku Yerusalemu kunali kotani?**
    Mbali ina kunali kuti Khristu adzabadwire mu dziko lalonjezano komanso kuti kutsimikize kusonkhanitsa kwa anthu ake a Mulungu mu mpingo wake wa muchipangano chatsopano. (monga Ezara 9; Nehemiya 8:1 – 9:38, Haggai 2:15-23; Masalimo 87; onaninso Luka 1:1 – 2:52)

Ndime zapamtima: Masalimo 122: 1-5

1. Ndinakondwera mmene ananena nane;
   Tiyeni ku nyumba ya Yehova.
2. Mapazi athu ali nkuima mzipata zanu, Yerusalemu
3. Yerusalemu anamangidwa ngati mudzi woundana bwino.
4. Kumene akwerako mafuko,
   ndiwo mafuko a Yehova; Akhale mboni ya maiko a kwa Israeli
   Ayamike dzina la Yehova.
5. Pakuti pamenepo anaika mipando ya chiweruzo,
   Mipando ya nyumba ya Davide.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

NTHAWI YACHISANU
KUKHALA KWA ISRAELI MU KANANI KUFIKIRA KUBADWA KWA KHRISTU

PHUNZIRO 23
MULUNGU ATETEZA ANTHU AKE APANGANO

1. **Kodi ndi buku lanji la mu buku loyera lomwe limakamba za Ayuda amene anatsalira ku Babulo?**
   Buku la Estere, lomwe linatchulidwa potengera dzina la mtsikana wachiyuda amene anadzakhala mfumukazi ya ku Persiya.

2. **Kodi choonadi chomwe chimakambidwa m'bukuli ndi chotani?**
   Chakuti oipawo sangathe kuthetsa ndi kuononga mpingo wa Mulungu. (monga Estere 8:7-11, 16-17)

3. **Kodi oipawo anayesetsa kuti awononge mpingo wa Yehova munthawiyi?**
   Inde, satana anagwiritsa ntchito Haman kuti ayesere kupha Ayuda. (Estere 3)

4. **Kodi Haman anafuniranji kuononga mpingo wa Mulungu?**
   Chifukwa anadana ndi Modekayi amene anali myuda. (Estere 3:1-6)

5. **Kodi anachita chiyani kuti ayuda onse aphedwe?**
   Anaumiriza mfumu Ahaswero kuti akhazikitse lamulo loti ayuda onse aphedwe. (Estere 3:8 mpaka kutsogoloko)

6. **Kodi Mulungu anagonjetsa bwanji maganizo a Hamani?**
   Mulungu anamugwiritsa ntchito Estere kuti apemphe moyo wake kuti usaonongedwe pamodzi ndi anthu ake. (Estere 7:1-4)

7. **Kodi ndani amene anamuuza Estere kuti apemphe moyo wake ndi wa anthu ake kuti asaphedwe?**
   Nsuweni wake wotchedwa Modekayi amene anamulera iye mu dera ili la osakhulupilira.

8. **Kodi Haman analandila kulangidwa kwanji?**
   Ananyongedwa pa makako amene anakonza kuti anyongere Modekayi. (Estere 7:7-10)

9. **Kodi linali tchimo kuti Ayuda monga Modekayi komanso Estere akhalebe ku ukapolo?**
   Inde, popeza sanawonetse kusangalatsidwa ndi Yerusalemu kumene mpingo unali, nyumba ya Yehova komanso ndi malonjezano a chipangano. (onani Ahebri 11: 8-10, 13-16; Eksodo 25:22; Rute 1:1-6, 19-21)

10. **Kodi tiphunzira chiyani pa mbiri imeneyi?**
    Tiphunzira kuti Mulungu anali wachikondi kwa anthu ake onse ndipo amatha kugwiritsa ntchito kuchimwa kwa anthu kuti apulumutse Mpingo wake. (Estere 8:1; 8:15 – 9:5; Yeremia 24:7)

Ndime zapamtima: Masalimo 122:6

6. Mupempherere mtendere wa Yerusalemu,
   akukonda inu adzaona phindu.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 24
TCHIMO LIONEKERANSO MU KANANI

1. **Kodi ndi ndani amene Mulungu anamutumiza kuti alimbikitse Ayuda kumanga zipupa za Yerusalemu komanso kukhala okhulupilira mwa Yehova?**
   Mlembi wotchedwa Ezara komanso Nehemiya amene anali wonyamula zikho za chifumu. (monga Nehemiya 2: 17-18; 3; 4:6; 8)

2. **Kodi Ayuda anakhala okhulupilika ndi omvera Mulungu pamene anabwelera ku Yerusalemu?**
   Ayi, zinaonekeratu kuti panali ambiri ochimwa pakati pawo.

3. **Kodi ndi machimo anji amene Ayuda anawachita?**
   Iwo anakwatira akazi achikunja ndikupanga malonda pa sabata. (Nehemiya 13:16, 23)

4. **Kodi ndi machimo anji amene ansembe anachita?**
   Ambiri a iwo anakwatira akazi achikunja nachitanso chinyengo ndi unsembe wawo. (Nehemiya 13:22, 28-29; Ezara 9: 1-3)

5. **Kodi ndi chifukwa chiyani Haggai anawadzudzula Ayudawa pa nthawiyi?**
   Chifukwa iwowa anadzimangira nyumba zokongola m'malo momanga nyumba ya Yehova. (Haggai 1: 1-5)

6. **Kodi Mneneri Malaki anawadzudzula Ayuda za chiyani?**
   Anawauza iwo kuti anali kumubera Mulungu mu zopereka zawo komanso nsembe zawo. (Malaki 3:8)

7. **Kodi tchimo limeneli pakati pa Ayuda likutiuza chiyani?**
   Litiphunzitsa kuti palibe mmodzi wa ife amene ayenera kulandila madalitso amene Mulungu akulonjeza ife kudzera mwa Khristu. (Mika 7)

8. **Kodi china ndi chiyani chimene tchimoli likutionetsa?**
   Kuti kunali kosatheka kuti Khristu abwere kupatula chozizwitsa cha chisomo chake.

9. **Kodi kulapa machimo kwa a Israeli ena kutionetsa chiyani?**
   Kuti Mulungu ndiwokhulupilika ku lonjezo lake lakuti mphukira yake ikhale tcheru ndi kubwera kwa Khristu. (Malachi 3:16)

10. **Kodi Mulungu analankhula bwanji za kukhulupilika kwake kudzera mwa Malaki?**
    Iye anati," pakuti ine Yehova sindisinthika ,chifukwa chake inu ana a Yakobo simunathedwa" (Malachi 3:6)

Ndime Zapamtima: Masalimo 122: 7-9

7. Mlinga mwako mukhale mtendere, m'nyumba mwa chifumu mukhale phindu
8. chifukwa cha abale anga ndi mabwenzi anga, ndidzanena tsopano, mukhale mtendere mwa inu.
9. Chifukwa cha nyumba ya Yehova Mulungu wathu ndidzakufunira zokoma.

Copyright © Gratia Dei Sola Media

PHUNZIRO 25
KUKONZEKERA KUBWERA KWA KHRISTU

1. **Kodi a Israeli anakhalanso ndi mfumu ina ya pansi pano pamene anabwerera kuchokera ku ukapolo?**
   Ayi, Israeli anali kulamulidwa ndi Persiya komanso Greece, ndipo mmasiku a Ambuye Yesu, anali kulamulidwa ndi ufumu wa Roma. (monga Luka 3:1; Machitidwe Atumwi: 2:9-11)

2. **Kodi Ayuda anadzilamulira okha munthawiyi?**
   Inde, kwa nthawi anali kulamulidwa ndi anthu otchedwa a Maccabees.

3. **Kodi ndi kupembedza kwanji kumene kunachuluka pamene anabwerera ku Kanani?**
   Ayuda anayamba kukhala mmasinagoge pa tsiku la sabata kuti awerenge ndi kufotokozera malamulo komanso kupemphera. (monga Mateyu 6:5; 9:35)

4. **Kodi chinthu chimene chinali kuchitika munthawi imene anabwerera ku Kanani kufikira kubwera kwa Khristu ndi chiyani?**
   Iyi inali nthawi imene anthu ambiri anazunzika chifukwa chokhulupilira komanso panali kuchitika zoipa zambiri mu nyumba ya Mulungu.

5. **Kodi chinachitika ndi chiyani pamene Ayuda anali kuphedwa ndi mafumu achikunjawa?**
   Ayuda anagawikana pa dziko lonse . (Machitidwe 2:9-11)

6. **Kodi Mulungu anafuniranji kuti ulamuliro wa ku Roma ulamulire anthu ake?**
   Kuti uthenga wabwino ufalikire ponseponse pamene Ambuye Yesu anafa ndi kuuka kwa akufa. (monga Machitidwe 10:1-8; Aroma 15:23-25)

7. **Kodi izi zinathandiza bwanji kufalitsa kwa uthenga wabwino wa Mulungu?**
   Dziko lonse linagwirizanika ndi chiyankhulo chimodzi ndipo atumwi anali kuyenda mopanda vuto kuchoka dziko lina kupita ku dziko lina.

8. **Kodi Mulungu sadanene kuti ndodo yachifumu siidzachoka ku Yuda kufikira Shiloh atabwera?**
   Inde, ndipo mbumba yachifumu ya Davide inasungika kufikira pamene Khristu anabadwa. (Luka 1:27, 32; 2:1-4)

9. **Kodi Khristu ndi Shiloh olonjezedwayo amene adzakhale pa mpando wachifumu wa Davide nthawi zonse**?
   Inde, iyeyu ndiye Mpulumutsi amene chipangano chakale chinalonjeza. (Genesesi 49:10; Yesaya 9:6-7)

10. **Kodi ndi chifukwa chiyani iyeyu akutchedwa kuti Shiloh?**
    Chifukwa iye akubweretsa kupambana pa adani athu onse ndikutipatsa ife mpumulo wosatha. (Yesaya 9:6; onaninso Masalimo 2)

Ndime Zoonjezera zapamtima: Masalimo 89: 1-4

1. Ndidzayimbira zachifundo za Yehova nthawi zonse, Pakamwa panga ndidzadziwitsira chikhulupiliko chanu ku mibadwo mibadwo.
2. Pakuti ndinati ,chifundo adzachimanga kosaleka; mudzakhala chikhulupiliko chanu m'mwamba mweni mweni.
3. Ndinachita chipangano ndi wosankhika wanga, ndinalumbira Davide mtumiki wanga.
4. Ndidzakhazika mbeu yako ku nthawi yonse, ndipo ndidzamanga mpando wachifumu wako ku mibadwo mibadwo.

Copyright © Gratia Dei Sola Media